

CHICHEWA – “Peace”

MTENDERE



“Ukadazindikira tsiku ili, inde iwetu zinthu zamtendere koma tsopano zibisika pamaso pako! (Luka 19:42)

Pamene tiyang'ana potizungulira ndi kuona zinthu zirinkuchitika m'dziko lapansi lero, tonse tiona kuti mulibe mtendere m'dziko lapansi. Kuli konse mumva za chidani, kumenyana, kuphana, nkondo ndi mbiri zokhudza nkondo. Palibe kanthu mukuwerenga nyuzipepala iti, koma monsemo mudzapezamo zochititsa mantha zomwe anthu alinkuchitirana chifukwa cha uchimo, udani ndi nsanje. Atsogoleri akulu-akulu adziko la pansi akhala akuyesetsa kubweretsa mtendere m'dziko lapansi koma onse alephera. Sikuti dziko lapansi liri pangosi yotere yokha ayi, komanso ndi chinthu chomvetsa chisoni kuchinena, kuti m'mabanja mwathunso mulibe mtendere. Choipa choposa pamenepo ndi ichi kuti pali chiwerengero chachikulu cha anthu padziko lapansi lero amaene alibe mtendere m'mitima mwawo ndipo uwu ndi muzu wa zovuta zonse.

CHIFUKWA CHIYANI PADZIKO PALIBE MTENDERE?

Pachiyambi Mulungu analenga dziko lapansi pamodzi ndi udzu, maluwa, mitengo ndi nyama zonse zokhala m'madzi ndi pamtunda zomwe. Mulungu adalenganso Adamu ndi Hava ndipo m'chilengedwe chonsechi mudali mtendere. Adamu, Hava ndi zinyama adali kukhala mwamtendere, mosaopana ndi mukondwera limodzi. Nkhosa zidali kuyenda pafupi ndi mkango popanda chovuta. Koposa zonse, panali mtendere pakati pa Mulungu ndi munthu ndipo Mulungu adali kubwera nthawi yamadzulo nayenda ndi kuyanahulana ndi Adamu ndi Hava. Iwe adalibe mantha m'mitima mwawo kuopa Mulungu ndipo iwo adali kuyang'anira kubwera kwacha kuti adzacheze nawo.

Tsopano Satana, ndiye adali mdani wa mtendere, ndipo analowa munjoka nanyenga Adamu ndi Hava kuti achimwe, pakuti kumene kuli uchimo kulibe mtendere. Satana tate wa mabodza, anawauza kuti sadzafa ngakhale akadapanda kumvera Mulungu nadya chipatso chimene Mulungu anawauza kuti asadye. Monga momwe anthu ambiri masiku ano amavera zonena Satana, momwemonso Adamu ndi Hava anamvera zonena Satana ndi kumuchimwira Mulungu. Nthawi yomweyo mtendere wawo unawachokera. Mtendere wonse ndi kukongola konse komwe Mulungu anawalenga nako kunawonongeka tsopano chifukwa cha uchimo, ndipo mantha analowa mumtima mwa Adamu ndi Hava.

Madzulo amene aja, pamene Mulungu anabwera, monga chinali chizolowezi chache, kudzayankhula nawo, lwo anabisala ndipo anali ndi mantha kuopa kuonana ndi Mulungu. "Chifukwa chache monga uchimo unalowa m'dziko mwa munthu m'modzi ndipo linabweretsa imfa, ndipo ngakhale ife amane tiri ndi moyo lero, TINACHIMWA ndi kuperewera pa ulemero wa Mulungu (Aroma 3:23 ndi Aroma 5:12). Nthawi zambiri uchimo umodzi umatsogolera ku unzache, ndipo lero dziko lonse lapansi liri lodwalika ndi uchimo. Chifukwa cha ichi palibe mtendere pa dziko lapansi.

MULUNGU ANAFUNA KUBWERETSANSO MTENDERE KUDZIKO LAPANSI

Mulungu anayang'ana padziko la pansu ndipo anaona udani, mantha, uchimo ndi chisoni, ndipo m'chikondi chache chachikulu anatumwiza Mwana wache wobadwa yekha kuti abadwire modyera ng'ombe, ndipo chaka ndi chaka pa nthawi ya Khirisimisi, timakumbutsidwa mawu amngelo uja "MUSAOPE" pakuti onani, ndikukuuzani inu Uthenga Wabwino wa chikondwerero chachikulu, chimene chidzakhala kwa anthu onse; pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Khirisitu Ambuye. Ndipo ichi ndi chizindikiro kwa inu: Mudzapenza Mwana wokhala wokuta ndi nsalu atagona modyera ng'ombe. Ndipo mwadzidzidzi, panali angelo ambirimbiri aguru la Kumwamba, amene ankatamanda Mulungu, nanena, Ulemero ukhale kwa Mulungu Kumwambamwamba, ndi mtendere pansu pano mwa anthu amene akondwera nawo (Luka 2:10-14). Yesu anatumidwa ku dziko lapansi lino kuti awalitsire iwo okhala mumtima ndi mthunzi wa imfa ndi kuwalunjikitsa mapanzi awo munjira ya mtendere (Luka 1:79). Komanso Aefeso 2:14 akutiuzanso kuti "Iye ndiye mtendere wathu" Mulungu anatumiza Kalonga wa Mtendere Yesu Khirisitu ku dziko lapansi, ndipo anthu masiku aja akadangomulandira Kalonga wa Mtendereyo akadakhalsanso mumtima monga kale.

KODI ANTHU ANACHITA NAWO CHIYANI MTENDEREWI-YESU KHIRISITU

Monga Adamu ndi Hava, Ayuda ndi anthu amitundu ndiponso anthu a nthawi ija,

anasankha kusamvera Mulungu natsata mawu a Satana. Anamukana Kalonga wa Mtendere ndipo pamene Pilato anawafunsa kuti asankhepo pakati mmodzi pakati pa Yesu ndi Baraba, iwo anafuula, “MPACHIKENI YESU!” Mutipatse Baraba! M'mawu ena tinganene kuti iwo ananena mawu otere: “MUCHOTSENI KALONGA WA MTENDERE NDIPO MUTIPATSE UDANI, NKHONDO, KUPHANA NDI UCHIMO.”

Anthu awa anali ndi ufulu wawo wakusankha ndipo akadadzisankhira wokha popanda kulumulidwa. Koma ngakhale kudali choncho, iwo anasankha BARABA. Masiku athu ano afanana ndi masiku akale aja. Mulungu watipatsa chisankho, tingathe kusankha YESU kuti akhale Mpulumutsi wathu, Mfumu yathu, ndipo lye adzabweretsa mtendere m'miyoyo yathu, ndipo lye akuti “Mtendere wanga ndikukusiyirani inu, mtendere wanga ndikukupatsani, ine sindikukupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa.” (Yohane 14:27). Machimo amene ali m'miyoyo yathu atitengera ife kutali ndi Mulungu ndipo ndi mkhalidwe wathu wochimwa tiribe mtendere mkati mwathu, koma nthawi zonse Yesu alinkuima ndi manja otambasuka kudikira kuti alandirenso ife m'khola lache, atiyeretse m'mwazi wache wa mtengo wapatali, kuti atipatse mphamvu yakukhala ana a Mulungu ndi kutipatsa mtendre.

Tikawerenga Aroma 5:1, Popeza tsono tayedwa wolungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye Wathu Yesu Khirisitu. Palibe chinthu chomwe chingatipatse ife mtendere padziko lapansi lino, ndalama, chuma kapena kukhala omveka, chakumwa kapena kukhala membala wa mpingo zonse sizingatipatse mtendere. Pali njira imodzi yolandilira mtendere ndiyo kubwera kwa Ambuye Yesu kudezera mkumvomereza machimo athu ndi kulapa. Ali wokhulupirika ndi wolungama lye kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama china chiri chonse. Mtendere umene YESU amatipatsa umapambana chidziwitso chonse (Afilipi 4:7). Mtendere umenewu sungafotokozeredwe ndi munthu koma tingathe kuumva m'miyoyo yathu ngati tiri olola kulisiya dziko ndi zinthu zake, kusiya uchimo ndi abwenzi wochimwa ndi kutembenukira kwa Ambuye Yesu ndi kumtumikira lye yekha. Nkutheka kukhala wopanda mtendere koma sitingathe kufa opanda mtendere, “Pakuti Umfumu wa Mulungu sukhalira chakudya ndi chakumwa, koma chilungamu mwa Mzimu Woyera.” (Aroma 14:17). Motero ngati tiribe mtendere wa Mulungu m'mitima yathu pamene tifa, ndiko kuti sitikalandidwa kumwamba kwacha kwamtendere. Ngati sitinamulandire Kalonga wa Mtendere m'miyoyo yathu ndipo tifa m'makhalidwe athu ochimwa, kuli malo amodzi okha komwe tidzapita ndiko ku moto wosatha wa Gehena. Simungathe kufa m'mene muli tsopano chifukwa mudzatayika kwa muyaya, ndipo mawu a Mulungu atiuza kuti “Utsi wa chilango chanu udzakwerabe mpaka nthawi ya muyaya, ndi ku Gehena wamuyaya kumene wochimwa adzapita. Ndipo tonse tinachimwa. Palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi. Chifukwa chache ngati mufuna kupita kumwamba, pali njira imodzi yokha ndiyo kupanga mtendere ndi Mulungu ndi kukhala nawo mtendere wa Mulungu mumtima mwanu. Ndipo mtendere wa Khirisitu uchite Ufunu mumtima mwanu (Akolose 3:15).

Pa nthawi ya Khirisimisi timakumbutsidwa za kubwera kwa Yesu kudzapereka mtendere ku dziko lapansi. Pa nthawi ya Easter timakumbutsidwa momwe anthu anamukana nampachika lye. Bwenzi langa, kod iwenso ufuna kukhala mmodzi wa iwo anamukana Ambuye, kapena mudzatsegula mtima wanu ndi kumulola lye alowemo? Pali njira imodzi yokha yakulandilira mtendere wa Mulungu mumtima mwanu, ndiyo yakugwada pamaso pa YESU, kuvomereza

kwa lye kuti muli ochimwa ndi kumufunsa lye akusambitseni m'mwazi wache wa mtengo wapatali ndi kukupangani mukhale wachewache; Palibe kanthu pa za ubwino umene mumaganiza mulinawo, mufunika mupulumutsidwe. Palibe kanthu za kuipa kumene muganiza muli nako, ali olola kukulandilani ndipo sathamangitsa munthu. Ngati musanalandire mtendere wa Mulungu m'moyo wanu, ulandireni tsopano ndipo mudzakhala ndi chimwemwe chosaneneka ndi chodzala ndi ulemerero (1 Petulo 1:8).

Tsiku lina pa nthawi ya mapemphero, munthu wina wachikulire anaimirira nati "Ndakhala ndili ndi moyo mu nthawi yoweruza mafumu anayi. Poyamba tinali ndi nkondo ndipo inali nthawi yoopsa ndithu. Mu nthawi ya mfumu ya chiwiri tinali mkati mwa njala yayikulu ndipo tinadya makoswe, udzu ndi nkhu. M'nthawi ya chitatu adani athu anatigonjetsa ndipo tinali akapolo awo. Koma nthawi yomweyo inadzatchinzera Mfumu ina, Mfumu yaikulu, Mfumu yabwino, Mfumu ya mtendere, Mfumu ya chikondi – YESU AMBUYE kuchokera kumwamba! lye wapambana tsopano, wagonjetsa mitima yathu motero tsopano tikukhala mumtendere ndi muzochuluka, ndipo posachedwapa tikuyembekeza bukhala naye Kumwamba.

Bwenzi langa, pereka moyo wako kwa YESU tsopano. Nthawi ino, leka njira yako yopita ku Gehena, tembenuka mtima ndipo mutumikire Mfumu ya Mafumu, Mbuye wa Ambuye. Udzaona KUTI ABWENZI AKO akusiyani koma kumbukirani kuti YESU anati "Onani Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano." Ndipo pomaliza, "Mtendere wa Khirisitu uchite Ufumu m'mitima yanu ndikuthandizani pazochita zanu." (Akolose 3:15)

M.R. Gschwend

The popular "Heart Book" with its soul-saving message is obtainable in over 500 languages. Many have found salvation even just by looking at the pictures.

Kindly write to us if you are able to assist us with further translations of our free Gospel literature, informing us of the language into which you could translate this Gospel literature. Your assistance would be appreciated.

If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers. **Our Heart of Man Book can now be downloaded in 480 different languages onto cell phones, tablets, etc from our website www.angp-hb.co.za.**

For **free** Gospel literature, books and tracts in over 540 languages, write to:

E-MAIL: info@angp.co.za

ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS

P.O. Box 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.

(A Gospel Literature Mission financed by donations)

(Reg. No. 1961/001798/08)